# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA CHITIPA M'DZINJA LA 2024/2025

## Nyengo ya dzinja la 2024-2025 Mwachidule

Nyengo ya mvula ya 2024-2025 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi La Nina wochepa mphamvu. La Nina ndi kuzizira koposa mlingo kwa madzi pakati cha kum'mawa kwa nyanja ya mchere ya Pacific. Izi zikhala chomwechi mpaka kumayambiriro a chaka cha 2025.

Boma la Chitipa likuyembekezeka kulandira mvula yochulukirapo kuyerekeza ndi chaka chatha ndipo ikhala ya mlingo wokhazikika kapena kuposera apo.

## October 2024




Nyengo ya dzinja dziko la Malawi imayamba mwezi wa October

Madera ambiri a boma la Chitipa akuyembekezeka kukhala opanda mvula m'mweziwu. Komabe mvula ya mlingo ochepera 20mm ikhoza kugwa madera ena ochepa.

## November 2024




Madera ambiri a kumwera m'bomali akuyembekezeka kulandila mvula ya mlingo osaposera 100mm yomwe ndi mlingo okhazikika. Madera a kwa Mfumu yaikulu Nthalire komanso ku Nyika National Park.Mvula ya pakati pa 100mm mpaka 150mm ikuyembekezeka kuyamba mu sabata yomaliza ya mwezi wa November mpaka sabata yachiwiri ya mwezi wa December

Mphepo ya mphamvu komanso mphenzi ikhoza kuchitika mwezi wu.

## December 2024




Mvula ya mlingo wa pakati pa 150mm mpaka 250mm ndi yomwe ikuyembekezeka mmadera ambiri a boma la Chitipa. Madera a mfumu yayikulu Mwenemisuku akuyembekezera kulandila mvula ya pakati pa 250mm-350mm

Mvula yobyalira ikuyembekezeka pakati pa sabata yomaliza ya mwezi wa November mpaka sabata yachiwiri ya mwezi wa December.

## January 2025




Mvula ya mlingo wa pakati pa 250mm mpaka 350mm ikuyembekezeka. Mmadera a mfumu yayikulu Nthalire komaso Nyika National Park mvula ya mlingo wa pakati pa 150mm mpaka 200mm ikuyembekezeka. Mvula imeneyi ndi mlingo wokhazikika ndi kuposera.

Ng'amba ya masiku osaposera asanu ndi atatu ikhoza kuchitika m'madera ena a bomali.

## February 2025




Mvula ikuyembekezeka kupitirira mu February. Mmadera ambiri a bomali akuyembekezera mvula yochulukirapo yopyolera mulingo wa 150mm .

Mmadera a mfumu yayikulu Mwenemisuku, Mwenewenya komaso Chitipa boma akuyembekezeka mvula yopyolera mulingo wa 200mm

Chiopsezo chan ng'amba ndi chochepa m'mweziwu ku Chitipa.

## March 2025




Mvula ya mlingo wa 250mmi kuyembekezeka pa boma lachitipa komaso mmadera mfumu yayikulu Mwenemisuku

Mmadera ambiri a m'bomali mwezi wa March akuyembekezeka mvula ya pakati pa 150mm mpaka 200mm.

## April 2025




Mvula ya mlingo wa pakati pa 100mm mpaka 150mm ikuyembekezeka kugwa m'bomali.

Nyengo ya dzinja ikuyembekezeka kufika kumapeto pakati pa sabata yomaliza ya mwezi wa March komaso sabata yachiwiri ya mwezi wa April 2025.

Mvula ikuyembekezeka kuyamba pakati pa sabata yotsiriza ya mwezi wa November mpaka sabata yachiwiri ya mwezi wa December 2024. Ng'amba yosapyola masiku asanu ndi atatu ikhoza kuchitika mwezi wa January 2025.

Nyengo yadzinja ikuyembekezeka kutha pakati pa sabata yotsiriza ya mwezi wa March 2025 ndi sabata yachiwiri mwezi wa April 2025.

Nyengo yonse yadzinja ikuyembekezeka kutalika pakati pa masiku 120 ndi 139.

Ndondomeko ya kagwedwe ka mvula ya pamwezi yaperekedwa m'munsimu.

| CHITIPA | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 0.0 | 0.2 | 7.7 |
| NOV | 40.2 | 82.0 | 24.1 |
| DEC | 152.0 | 245.7 | 202.3 |
| JAN | 196.6 | 265.3 | 277.3 |
| FEB | 177.3 | 251.8 | 188.1 |
| MAR | 133.0 | 204.5 | 174.4 |
| APR | 22.7 | 71.7 | 134.4 |




**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**

**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**

The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.

Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: